# MONJOLE COMMUNITY PRIMARY SCHOOL

## 2021/2021PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMS

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Subject Number: P032**
**Time allowed: 2h 15 mins**

**Dzina lanu:** ________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** ________________________________

## Malangizo:

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi limodzi.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C ndi D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D.**
6. Lembani yankho la mu **Gawo A** pa pepala lapadera lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu gawoli.
7. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
8. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozuguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.
9. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake
10. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso **(Imvijireta)** pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 – 8 | | | |
| 9 – 15 | | | |
| 16 – 18 | | | |
| 19 – 20 | | | |
| 21 – 25 | | | |
| 26 – 30 | | | |
| 31 – 35 | | | |
| 36 – 39 | | | |
| 40 – 41 | | | |
| 42 – 43 | | | |
| 44 – 45 | | | |

**Onani paseri**

GAWO A (Malikisi 30)

Yakhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu; NKHALANGO YATHU. Mwazina tsatani izi polemba;

   **Ndime yoyamba**
   - Dzina la nkhalango
   - Dera lomwe nkhalangoyo ili
   - Kukula kwa nkhalangoyo

   **Ndime yachiwiri**
   - Mitundu yamitengo yopezeka munkhalangoyo
   - Kufunika kwa nkhalangoyo

   **Ndime yachitatu**
   - Momwe anthu amderalo akusamalira nkhalangoyo

**KALPENA**

2. Lembani kalata kwa mnzanu yemwe mumaphunzira naye sukulu kumudziwitsa m'mene mudayendera ulendo wopita ku tchuthi.

   **Ndime yoyamba**
   - Sukulu mudatsekela liti
   - Ulendo wa kutchuthi mudanyamuka liti
   - Mudanyamuka ndi yani
   - Mudakwera chiyani pa ulendowo

   **Ndime yachiwiri**
   - Fotokozani zovuta ziwiri zomwe mudakumana nazo pa ulendo wanu
   - Zosangalatsa ziwiri zomwe mudaziona pa ulendowo
   - Mudanyamula chiyani pa ulendowo

   **Ndime yachitatu**
   - Adakulandirani bwanji komwe mudapitako
   - Zinthu zomwe zidasonyeza kuti adakulandirani bwino kapena ayi ndi chiyani
   - Tsiku lomwe mukuyembekezera kubwereranso

## GAWO B (Malikisi 20)

**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengani nkhani ili m'munsiyi kenako muyankhe mafunso otsatirawo

Padali mudzi wina wotchedwa Sinsamala womwe mudali banja lina la litsiro losaneneka. Banja limeneli lidali la bambo Sauzika ndi mayi Namoyo. M'banjamo Namalenga adawadalitsamo ndi ana atatu; amuna awiri ndi wamkazi m'modzi; Chitsekulira mawere adali Zilotho ndi chitseka mawere adali Nasimbenji.

Asauzika ndi a Namoyo adali aulesi wadzaoneni ndipo sadathe kuphunzitsa ana awo aja ntchito zosiyanasiyana. Anawo sadakule ndi makhalidwe abwino, kawirikawiri amagona ndi njala, moti Mkambana, Zilotho ndi Nasimbenji amangokhalira kudya m'makomo mwa anthu ena mpaka adafika poti anthu m'mudzimo adatopa nawo ana aja. Anthu amati akawaona ana aja amawapitikitsa ngati agalu. Pofuna kunena za m'nyumba mwawo ayi ndinthu mudali mosasamala ndipo adalibe chimbuzi. Zinyalala zidapeza nkhuti panja pa nyumba yawoyo.

Ntchntche nazo zimangoti ng'wang'wa chifukwa chosasamala pakhomo pawo pamapezeka kuti nthawi yamvula matenda samatha phazi pakhomo pagwo. Kolera, kamwazi, kankhombe ndi njika zidamanga nthenje pakhomopo. A Namoyo nthawi zambiri ndiye adali bwenzi la mphasa. Ana ajanso adalibe nthawi yosamba ndipo zovala zawo zimanunkha chikhwekhwezi.

Mwamwayi, tsiku lina kudabwera mlangizi wa zaumoyo, a Mangamudzi. Mayi Namoyo adauza mlangiziyo kuti ana awo adali bwenzi lamphasa ndipo amaonda. A Mangamudzi adawauza kuti; "Poyumba pafunika payende chiseso, akhale ndi chimbuzi komanso dzenje lotayilako zinyalala. Akatero zonsezi zidzakhala mbiri yakale." Adawafotokozeranso kuti ayenera kukhala ndi chakudya chokwanira. A Namoyo adamva malangizowa koma sadathe kuphunzitsa anawo chifukwa adali atawalekelera kale. Asauzika chifukwa cha manjalende adalephera kuchita zomwe a Mangamudzi adawauza. Banja lawo lidapitilira kukhala ndi matenda kholophethe pakhomopo.

Tsopano yakhani mafunso otsatirawa

a) Kodi banja la Sauzika limakhala kuti?
_______________________________________________ (Malikisi 1)

b) Banjali lidali ndi ana angati?
_______________________________________________ (Malikisi 1)

c) Tchulani zinthu ziwiri zosonyeza kuti banja la a Sauzika lidali la umve
_______________________________________________
_______________________________________________ (Malikisi 2)

d) N'chifukwa chiyani a Sauzika ndi a Namoyo sadaphunzitse ana awo ntchito?
_______________________________________________
_______________________________________________ (Malikisi 2)

e) Perekani matanthauzo a zining'a zotsatirazi molingana ndi nkhaniyi?
i) Bwenzi lamphasa _______________________________ (Malikisi 1)
ii) Sathaphazi _______________________________ (Malikisi 1)

f) Tchulani vuto limodzi lomwe banjali limakumana nalo
_______________________________________________ (Malikisi 2)

g) Perekani malangizo awiri omwe a Namoyo adauzidwa ndi a zaumoyo?
_______________________________________________
_______________________________________________ (Malikisi 2)

h) Kodi dzina loti, "Sauzika" ndi zochitika M'nkhaniyi zikugwirizana motani?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________ (Malikisi 2)

i) Lembani mimvekero iwiri m'khaniyi

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________ (Malikisi 2)

j) Pezani mawu m'nkhaniyi otsutsana m'matanthauzo ndi awa

i) Adapita ______________________________________________________ (Malikisi 1)

ii) M'dani ______________________________________________________ (Malikisi 1)

k) Perekani mutu wankhaniyi

______________________________________________________________________ (Malikisi 2)

**GAWO C (Malikisi 10)**

Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

4. a) A phiri : odi! Odi!
A Nanyoni : Eee! Tikuopeni, bamboo?
A Phiri : Musandiope kwenikweni. Kodi amuna anu alipo?
A Nanyoni : Ayi, palibe. Mwomwe achokera m'mawa.
A Phiri : Chabwino sindivutika popeza inu mulipo. Mawa kuli liwamba. Nachi chimanga chofiira mudzawapatse amuna anu.

Mafunso

i) Kodi ndi uthenga wanji womwe a Phiri abweretsa?

______________________________________________________________________ (Malikisi 1)

ii) Kodi m'malonjewa, a Phiri ndi ndani?

______________________________________________________________________ (Malikisi 1)

iii) Naga chimanga chofila chimatanthauzanji m'malonjewa?

______________________________________________________________________ (Malikisi 1)

b) N'chifukwa chiyani achinyamata amayenera kuvula chipewa pakati pa akuluakulu?

______________________________________________________________________ (Malikisi 1)

c) Ndiyani yemwe amalangiza amfumu m'mudzi

______________________________________________________________________ (Malikisi 1)

5. Kupanga Ziganizo

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa.

a. Phe ______________________________________________________________

______________________________________________________________________

b. Khwasula __________________________________________________________

______________________________________________________________________

c. Balamanthu ________________________________________________________

______________________________________________________________________

d. Chiwembu __________________________________________________________

______________________________________________________________________

e. Ngati ______________________________________________________________

______________________________________________________________________

## GAWO D (Malikisi 40)

***Mafunso 6 mpaka 10:* Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

6. Katangale ndi woipa
   A. Mlumikizi
   B. Mvekero
   C. Mperekezi
   D. Mneni
7. Iye wapiti kwa achimwene ake mawa.
   A. Mvekero
   B. Mperekezi
   C. Muonjezi
   D. Mlumikizi
8. Maphunziro ndi ofunika m'dziko lililonse
   A. Dzina
   B. Muonjezi
   C. Mneni
   D. Mlowam'malo
9. Munthu uja akudwala malungo
   A. Mfotokozi
   B. Mlowam'malo
   C. Mlumikizi
   D. Muonjezi
10. Ndidzapita kumudzi ndikakhoza mayeso.
    A. Mvekero
    B. Mlumikizi
    C. Mlowammalo
    D. Muonjezi

***Mafunso 11 mpaka 15:* Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi**

11. Fisi wagwira mbuzi
    A. Loitanira
    B. Mtsirizo wamneni
    C. Mwininkhani
    D. Pamtherankhani
12. Pangaunye, Sing'anga wam'mudzi muno wabwera
    A. Lapadera kudzina lina
    B. Loitanira
    C. Pamtherankhani
    D. Pamtherankhani wamperekezi
13. Talandira, bwera kuno
    A. Pamtherankhani
    B. Mwininkhani
    C. Mtsirizo wamneni
    D. Loitanira
14. Mwana akusewera mpira
    A. Mwininkhani
    B. Pamtherankhani
    C. Mtsirizo wamneni
    D. Pamtherankhani wamperekezi
15. Joni si mzanga
    A. Pamtherankhani
    B. Mtsirizitsi wamneni
    C. Mwininkhani
    D. Loitanira

***Mafunso 16 ndi 17:* Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi**

16. Ku gomo ilo kuli njoka zambiri.
    A. Dera
    B. Manda
    C. Phiri
    D. Chigwa
17. Utchisi ndiofunika pasukulu
    A. Ukhondo
    B. Ulamuliro
    C. Usiwa
    D. Uve

***Mafunso 18 mpaka 22;* Sankhani nthawi za aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.**

18. Anthuwo adali ochepa
    A. Yakale
    B. Yatsopano
    C. Yamtsogolo
    D. Yakawirikawiri
19. Atsikana akuphika nyemba
    A. Yakawirikawiri
    B. Yakale
    C. Yamtsogolo
    D. Yatsopano yopitilira
20. Ife tizidzabwera mukadzakwatirana
    A. Yamtsogolo
    B. Yakale
    C. Yamtsogolo
    D. Yatsopano yopitilira
21. Iwo adya nsima
    A. Yathayi
    B. Yakawirikawiri
    C. Yopitilira

D. Yakale

22. Ine <u>ndidzidzapitapita</u> ku Lilongwe.
   A. Yatsopano
   B. Yakale
   C. Yakawirikawiri
   D. Yathayi

***Mafunso 23 mpaka 27*: Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe**

23.
   A. Eya, wajowa bwino.
   B. Eya! Wajowa bwino.
   C. Eya! Wajowa bwino.
   D. Eya! Wajowa bwino?

24.
   A. Mwana walowa m'sitolo.
   B. Mwana walowa m'sitolo
   C. Mwana walowa sitolo.
   D. Mwana walowa msitolo

25.
   A. A bambo akufuna iz: mpando, chikwama, mwana ndi mbale.
   B. A bambo akufuna izi: mpando, chikwama, mwana ndi mbale.
   C. A bambo akufuna izi; mpando, chikwama, mwana, ndi mbale.
   D. Abambo akufuna izi; mpando, chikwama, mwana ndi mbale.

26.
   A. Ha, kaledi silibwerera.
   B. Ha kaledi salibwerera.
   C. Ha! Kaledi silibwerera.
   D. "Ha!" Kaledi silibwerera.

27.
   A. Aphunzitsi adati, "Muzilimbikira sukulu ananu."
   B. "Aphunzitsi adati, muzilimbikira sukulu ananu."
   C. "Aphunzitsi adati muzilimbikira sukulu ananu."
   D. "Aphunzitsi adati! Muzilimbikira sukulu ananu."

***Mafunso 28 mpaka 32:* Sankhani gulu la mayina a mawu omwe ali m'musiwa**

28. Kubwalo
   A. Ku -, pa -, Mu –
   B. Mu -, A –
   C. Mu -, Mi –
   D. U -, Ma -

29. Maulalo
   A. U -, Ma –
   B. Ka -, Ti –
   C. Chi -, Zi-
   D. Li -, Ma -

30. Chikwama
   A. I -, Zi –
   B. Chi -, Zi –
   C. Li -, Ma –
   D. U -, Ma -

31. Ndege
   A. U -, Ma –
   B. I -, Zi –
   C. Chi -, Zi –
   D. Mu -, A -

32. Khasu
   A. Chi -, Zi –
   B. U -, Ma –
   C. Li -, Ma –
   D. Mu -, Mi –

***Mafunso 33 mpaka 37:* Sankhani mitundu ya nthambi zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo**

33. <u>Zoti adapita kusukulu</u> ndi zoona
   A. Ya muonjezi
   B. Yadzina
   C. Yamfotokozi
   D. Yoima payokha

34. Iwo amakonda dziko <u>lomwe kuli mtendere</u>
   A. Yamuonjezi
   B. Yamfotokozi
   C. Yoima payokha
   D. Yadzina

35. Mwanayo amayenda <u>ngati akudwala</u>.
   A. Yamfotokozi
   B. Yamuonjezi
   C. Yadzina
   D. Yoima payokha

36. Sindikudziwa <u>chimene akuvutikira</u>.
   A. Yadzina
   B. Yamfotokozi
   C. Yoima payokha
   D. Yamuonjezi

37. Adzabwera <u>pokhapokha mudzamuyitane</u>.

A. Yoyima payokha
B. Ya muunjezi
C. Yamfotokozi
D. Yadzina

***Mafunso 38 mpaka 42:* Sankhani mitundu ya alumikizi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

38. Atsibweni andipatsa njinga ndi buku
    A. Wadzina
    B. Wamneni
    C. Wamuonjezi
    D. Wamfotokozi
39. A Phiri amadwala ndipo achira
    A. Wamuonjezi
    B. Wamneni
    C. Wadzina
    D. Wamfotokozi
40. Amayi akulima mwanyonga ndi mwamphamvu
    A. Wadzina
    B. Wamfotokozi
    C. Wamneni
    D. Wamuonjezi
41. Mnyamata wamtudzu ndi waulesi amamvetsa chisoni makolo
    A. Wamuonjezi
    B. Wamneni
    C. Wamfotokozi
    D. Wadzina
42. Agogo ndi ana akukambirana nthano
    A. Wadzina
    B. Wamuonjezi
    C. Wamfotokozi
    D. Wamneni

Mafunso 43 mpaka 45; Tsirizitsani mikuluwiko yotsatirayi

43. Nkhuyu zodya ___ zidapota akulu
    A. mnyamata
    B. mwana
    C. msungwana
    D. mkamwini
44. Madoli adafera ___ woyera
    A. mkanda
    B. madzi
    C. mchenga
    D. mkazi
45. Nkhanga zidapangana _______
    A. kusanapse
    B. kutacha
    C. kusanache
    D. m'mawa

**MAFUNSO ATHERA APA!!**